# Pali Njira ya Bwino



## Kodi mwakhumudwa ndi kubvutika?

Yesu Kristu adzakulimbikitsani ndi kukutonthozani. "Ndikukusiyirani mtendere. Ndikupatsani mtendere wanga. Sindikupatsani mtenderewo monga mmene dziko lino lapansi limapatsira ayi. Mtima wanu usabvutike kapena kuda nkhawa." Yohane 14:27

## Kodi muli osakondwa ndi okhumudwa?

Yesu Kristu adzakupatsani chimwemwe. "Mudzandidziwitsa njira ya moyo; pankhope panu pali chimwemwe chokwanira; m'dzanja lanu lamanja muli zokondweretsa zomka muyaya." Masalimo 16:11

## Kodi muli otopa ndi ofooka?

Yesu Kristu adzakupatsani mpumulo. "Bwerani kwa ine, inu nonse otopa ndi olemedwa, ndipo ine ndidzakupumitsani." Mateyu 11:28

## Kodi muli ndi mantha?

Yesu Kristu adzakupatsani kulimba mtima. "Usaope, pakuti ine ndiri pamodzi ndi iwe usaopsyedwe, pakuti ine ndine Mulungu wako; ndidzakulimbitsa, inde, ndidzakuthangata, inde ndidzakuchirikiza ndi dzanja langa lamanja lachilungamo." Yesaya 41:10

## Kodi muli nikha opanda bwenzi?

Yesu Kristu adzakhala bwenzi lanu. "...pakuti Mulungu anati, sindidzakusiyani kapena kukutayani konse." Aheberi 13:5

## Kodi mwalemedwa ndi katundu wa uchimo?

Yesu Kristu adzakukhululukirani. "Ndi imfa ya mwana wakeyo Mulungu anatipulumutsa, ndipo anakhululukira zolakwa zathu. Mwakukoma mtima kwake kwakululu." Aefeso 1:7

## Kodi mukudwala m'thupi?

Yesu Kristu adzakuchiritsani. "Akapemphera ndi chikhulupiriro, wodwalayo adzachira. Ambuye adzamuutsa, ndipo ngati anali atachimwa, Ambuye adzamkhululukira machimowo." Yakobo 5:15

## Yesu Kristu anabwera kudzakupatsani njira yabwino.

"Yesu anamuyankha kuti, Ine ndine njira, ndine choona ndiponso moyo. Palibe munthu angadze kwa Atate ngati sadzera mwa ine." Yohane 14:6

**Landirani Yesu Kristu monga mpulumutsi wanu lero.**

"Komabe anthu onse amene anamulandira ndi kumkhulupirira, Iye anawapatsa mphamvu yokhala ana a Mulungu." Yohane 1:12

**Tiyeni tipemphere:**

Okondeka Ambuye Yesu, ndazindikira kuti pali njira yabwino ndipo ndikufuna kuyenda mmenemo. Ndikulapa machimo anga ndikukul andirani monga mpulumutsi ndi Ambuye wanga.

**Lero ndalandira Yesu Kristu monga mpulumutsi wanga.**

Dzina ______________________________

Tsiku ______________________________

There Is A Better Way — Chichewa
Foursquare Missions Press © 2005